# Maphunziro a m'Baibulo

Bible studies

# Nehemiya

1. Nehemiya apempherera ana a lsrayeli kwa Mulungu
2. Adani ayesa kuwaletsa kumanga malinga
3. Adani ayesa kunyenga ndi kuopsa Nehemiya
4. Tsiku la Sabata likhalanso lopatulika

# 1. Nehemiya apempherera ana a lsrayeli kwa Mulungu

**Nehemiya 1**

1Mau a Nehemiya mwana wa Hakaliya. Kunali tsono mwezi wa Kisilevi, caka ca makumi awiri, pokhala ine ku Susani ku nyumba ya mfumu,
2anafika Hanani, mmodzi wa abale anga, iye ndi amuna ena a ku Yuda; ndipo ndinawafunsa za Ayuda adapulumukawo otsala andende, ndi za Yerusalemu. 3Nanena nane iwo, Otsalawo otsala andende uko ku dzikoko akulukutika kwakukuru, nanyozedwa; ndi linga la Yerusalemu lapasuka, ndi zipata zace zatenthedwa ndi moto.
4Ndipo kunali, pakumva'mau awa, ndinakhala pansi ndi kulira misozi, ndi kucita maliro masiku ena, ndinasalanso, ndi kupemphera pamaso pa Mulungu wa Kumwamba,
5ndi kuti, Ndikupembedzani Yehova, Mulungu wa Kumwamba, Mulungu wamkuru ndi woopsa, wakusunga pangano ndi cifundo ndi iwo akumkonda ndi kusunga malamulo ace;
6muchere khutu, ndi maso anu atseguke kumvera pemphero la kapolo wanu, ndilipempha pamaso panu tsopano apa msana ndi usiku, kupempherera ana a Israyeli akapolo anu, ndi kuulula zoipa za ana a Israyeli zimene tacimwira nazo Inu; inde tacimwa, ine ndi nyumba ya atate wanga.
7Tacita mwamphulupulu pa Inu, osasunga malamulo, kapena malemba, kapena maweruzo, amene mudalamulita mtumiki wanu Mose.
8Mukumbukile mau mudalamulira mtumiki wanu Mose, ndi kuti, Mukalakwa, ndidzakubalalitsani mwa mitundu ya anthu;
9koma mukabwerera kudza kwa Ine, ndi kusunga malamulo anga, ndi kuwacita, angakhale otayika anu anali ku malekezero a thambo, ndidzawasonkhanitsa kucokera komweko, ndi kubwera nao ku malo ndinawasankha kukhalitsako dzina langa.
10Ndipo awa ndi akapolo anu ndi anthu anu, amene munawaombola ndi mphamvu yanu yaikuru, ndi dzanja lanu lolimba.
11Yehova, mucherere khutu pemphero la kapolo wanu, ndi pemphero la akapolo anu okondwera nako kuopa dzina lanu; ndipo mulemereze kapolo wanu lero lino, ndi kumuonetsera cifundo pamaso pa munthu uyu. Koma ndinali ine wothirira mfumu cakumwa cace.

**Nehemiya 2.1-10**

1Koma kunacitika mwezi wa Nisana, caka ca makumi awiri ca Aritasasta mfumu pokhala vinyo pamaso pace, ndinatenga vinyoyo ndi kuipatsa mfumu. Koma sindidakhala wacisoni pamaso pace ndi kale lonse.
2Ninena nane mfumu, Nkhope yako nja cisoni cifukwa ninji popeza sudwala? ici si cinthu cina koma cisoni ca mtima. Pamenepo ndinacita mantha akuru.
3Ndipo ndinati kwa mfumu, Mfumu ikhale ndi moyo kosatha; ilekerenji nkhope yanga kucita cisoni, popeza pali bwinja kumudzi kuli manda a makolo anga, ndi zipata zace zopsereza ndi moto.
4Ndipo mfumu inati kwa ine, Ufunanji iwe? Pamenepo ndinapemphera Mulungu wa Kumwamba.
5Ndipo ndinati kwa mfumu, Cikakomera mfumu, ndi mtima wanu ukakomera kapolo wanu, munditumize ku Yuda ku mudzi wa manda a makolo anga, kuti ndiumange.
6Ninena nane mfumu, irikukhala pansi pamodzi ndi mkazi wace wamkuru, Ulendo wako ngwa nthawi yanji, udzabweranso liti? Ndipo kudakonda mfumu kunditumiza nditaichula nthawi.
7Ndinanenanso kwa mfumu, Cikakomera mfumu, indipatse akalata kwa ziwanga za tsidya lija la mtsinje, andilole ndipitirire mpaka ndifikira ku Yuda;
8ndi kalata kwa Asafu wosunga misitu ya mfumu, kuti andipatse mitengo ya mitanda ya ku zipata, za linga liri kukacisi, ndi ya linga la mudzi, ndi ya nyumba imene ndidzalowamo ine. Ndipo mfumu inandipatsa monga mwa dzanja lokoma la Mulungu londikhalira.
9Ndinafika tsono kwa ziwanga za tsidya lino la mtsinje, ndipo ndinawapatsa akalata a mfumu. Koma mfumu idatumiza apite nane akazembe a nkhondo, ndi apakavalo.
10Atamva Sanibalati Mhoroni, ndi Tobiya kapoloyo M-amoni, cidawaipira kwakukuru, kuti wadza munthu kuwafunica ana a Israyeli cokoma.

**Mafunso**

1. Kodi mzinda wa Yerusalemu unali otani ndi anthu amene anakhalako anali bwanji kulingana ndi Nehemiya 1.3?
2. Kodi Nehemiya anacita ciani pamene anamva za Yerusalemu ndi anthu amene anakhalako? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Fotokozerani pemphero la Nehemiya.
4. Kodi mumapemphera motani?
5. Mfumu inaona kuti Nehemiya mtumiki wake anamva cisoni (Nehemiya 2.2). Kodi Nehemiya anafotokoza zimene zinamdzetsa cisoni? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi Nehemiya anacita ciani asanafunse mfumu kuti aloledwe kupita ku Yuda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi mumapemphera ngati mufuna thandizo la Mulungu?
8. Ndani amene sanali osangalala pamene Nehemiya anafika ku dziko la Yerusalemu kuthandiza anthu amene anakhalako? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

**Sewero**

Pezani mau onse ndipo lembani yankho

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | K | H | O | P | E | O | T | O | M |
| E | A | P | A | K | A | V | A | L | O |
| H | G | M | U | U | M | O | S | E | S |
| E | N | L | A | B | M | U | Y | N | A |
| M | I | S | O | Z | I | U | U | N | M |
| I | L | G | O | D | N | U | F | I | C |
| Y | E | R | U | S | A | L | E | M | U |
| A | U | P | E | M | P | H | E | R | O |

- Nehemiya
- misozi
- mfumu
- linga
- nyumba
- maso
- nkhope
- Yerusalemu
- cifundo
- pemphero
- apakavalo
- moto

Yankho:……………………………………

# 2. Adani ayesa kuwaletsa kumanga malinga

**Nehemiya 2.11-20**
11. Motero ndinafika ku Yerusalemu, ndi kukhalako masiku atatu.
12. Ndipo ndinauka usiku, ine ndi amuna owerengeka nane, osauza munthu yense ine coika Mulungu wanga m'mtima mwanga ndicitire Yerusalemu; panalibenso nyama yina nane, koma nyama imene ndinakhalapo.
(…)
16. Koma olamulira sanadziwa uko ndinamuka, kapena cocita ine; sindidauzenso kufikira pamenepo Ayuda, kapena ansembe, kapena aufuru, kapena olamulira, kapena otsala akucita nchitoyi.
17. Pamenepo ndinanena nao, Muona coipa m'mene tirimo, kuti Yerusalemu ali bwinja, ndi zipata zace zotentha ndi moto; tiyeni, timange linga la Yerusalemu, tisakhalenso cotonzedwa.
18. Ndinawauzanso za dzanja la Mulungu wanga londikhalira mokoma, ndiponso za mau anandiuza mfumu. Nati iwo, Tinyamuke, timange. Cotero anandilimbitsira manja mokoma.
19. Koma Sanibalati Mhoroni, ndi Tobiya kapolo M-amoniyo, ndi Gesemu M-arabu, anamva natiseka pwepwete, natipeputsa, nati, Ciani ici mucicita? Mulikupandukira mfumu kodi?
20. Koma ndinawabwezera mau, ndi kunena nao, Mulungu Wam'mwamba, Iye ndiye adzatilemeza; cifukwa cace ife akapolo ace tidzanyamuka ndi kumanga; koma inu mulibe gawo, kapena ulamuliro, kapena cikumbukilo, m'Yerusalemu.

**Nehemiya 3**
1. Ndipo kunali, atamva Sanibalati kuti tinalikumanga lingali, kudamuipira, nakwiya kwakukuru, naseka Ayuda pwepwete.
2. Nanena iye pamaso pa abale ace ndi ankhondo a ku Samariya, nati, Alikucitanji Ayuda ofokawa? adzimangire linga kodi? adzapereka nsembe kodi? adzatsiriza tsiku limodzi kodi? adzakometsanso miyala ya ku miunda yotenthedwa?
3. Ndipo Tobiya M-amoni anali naye, nati, Cinkana ici acimanga, ikakwerako nkhandwe, idzagamula linga lao lamiyala.
4. Imvani, Mulungu wathu, popeza tanyozeka ife; muwabwezere citonzo cao pamtu pao, ndi kuwapereka akhale cofunkhidwa m'dziko la ndende;
5. ndipo musakwirira mphulupulu yao, ndi kulakwa kwao kusafafanizike pamaso panu; pakuti anautsa mkwiyo wanu pamaso pa omanga linga.

6. Koma tinamanga lingali, ndi linga lonse linalumikizana kufikira pakati mpakati; popeza mitima ya anthu inalunjika kunchito.
7. Koma kunali, atamva Sanibalati, ndi Tobiya, ndi Aarabu, ndi Aamoni, ndi Aasidodi, kuti makonzedwe a malinga a Yerusalemu anakula, ndi kuti mopasuka mwace munayamba kutsekeka, cidawaipira kwambiri;
8. napangana ciwembu iwo onse pamodzi, kudzathira nkhondo ku Yerusalemu, ndi kucita cisokonezo m'menemo.
9. Koma tinapemphera kwa Mulungu wathu, ndi kuwaikira olindirira usana ndi usiku, cifukwa ca iwowa.
10. Ndipo Ayuda anati, Mphamvu ya osenza akatundu yatha, ndi dothi licuruka, motero sitidzakhoza kumanga lingali.
11. Nati adani athu, Sadzadziwa kapena kuona mpaka talowa pakati pao, ndi kuwapha, ndi kuleketsa nchitoyi.
12. Ndipo kunali, atafika Ayuda okhala pafupi pao ocokera pamalo ponse, anatiuza ife kakhumi, Bwererani kwa ife.
13. Cifukwa cace ndinawaika potera m'kati mwa linga, popenyeka; inde ndinaika anthu monga mwa mabanja ao, akhale nao malupanga ao, nthungo zao, ndi mauta ao.
14. Ndipo ndinapenya, ndinanyamuka, ndinanena kwa aufulu, ndi olamulira, ndi anthu otsala, Musamawaopa iwo; kumbukilani Yehova wamkuru ndi woopsa, ndi kuponyera nkhondo abale anu, ana anu amuna ndi akazi, akazi anu, ndi nyumba zanu.
15. Ndipo kunali, pakumva adani athu kuti cinadziwika nafe, ndi kuti Mulungu adapititsa pacabe uphungu wao, tinabwera tonse kumka kulinga, yense ku nchito yace.
16. Ndipo kuyambira pamenepo gawo lina la anyamata anga anagwira nchito, ndi gawo ina linagwira nthungo, zikopa, ndi mauta, ndi maraya acitsulo; ndi akuru anali m'mbuyo mwa nyumba yonse ya Yuda.
17. Iwo omanga linga, ndi iwo osenza katundu, posenza, anacita ali yense ndi dzanja lace lina logwira nchito, ndi lina logwira cida;
18. ndi omanga linga ali yense anamangirira lupanga lace m'cuuno mwace, nagwira nchito motero. Ndipo woomba lipenga anali ndi ine.
19. Ndipo ndinati kwa aufulu, ndi olamulira, ndi anthu otsala, Nchito ndiyo yocuruka ndi yacitando, ndi ife tiri palace palace palingapo, yense azana ndi mnzace;
20. pali ponse mukumva mau a lipenga, musonkhanire komweko kwa ife; Mulungu wathu adzatigwirira nkhondo.
21. Momwemo tinalikugwira nchito; gawo lina la iwo linagwira nthungo kuyambira mbanda kuca mpaka zaturuka nyenyezi.

22. Ndinanenanso kwa anthu nthawi yomweyi, Ali yense agone m'Yerusalemu pamodzi ndi mnyamata wace, kuti atilindirire usiku, ndi kugwira nchito usana.
23. Ndipo ine, ndi abale anga, ndi anyamata anga, angakhale amuna olindirira onditsata ine, nnena mmodzi yense wa ife anabvula zobvala zace, yense anapita ndi cida cace kumadzi.

**Mafunso**

1. Ndani amene anafika m'Yerusalemu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
2. Nehemiya anayendera Yerusalemu usiku. Kodi ataona Yerusalemu anaganiza kuti acite ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Ndani amene sanali osangalala kuti Nehemiya anabwera kumanga linga? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Ayuda anayamba kumanganso Yerusalemu. Kodi Sanibalati ndi Tobiya ananena ciani kunyozera Ayuda? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi anapanga ciwembu cotani kulingana ndi Nehemiya 4.8?
6. Kodi Ayuda anacita ciani atamva kuti adani awo anafuna kuwaononga? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
7. Kodi Nehemiya anati ciani kwa anthu ake kuti iwo alimbikitsidwe kulingana ndi ndime ya 14?
8. Kodi tingacite kapena tingakambe ciani kwa iwo amene aopa cifukwa ca mabvuto m'umoyo wao?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

Yehova anati m'Zekariya 2.15:

| | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | |
| 14 | 4 | 9 | 4 | 26 | 1 | 11 | 8 | 1 | 12 | 1 |

| | | |
|---|---|---|
| | | |
| 11 | 24 | 1 |

| | | |
|---|---|---|
| | | |
| 9 | 25 | 5 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |
| 12 | 9 | 14 | 7 | 1 |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |
| 12 | 1 | 13 | 15 | 20 | 15 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| **A** 1 | **B** 2 | **C** 3 | **D** 4 | **E** 5 | **F** 6 | **G** 7 | **H** 8 | **I** 9 | **J** 10 | **K** 11 | **L** 12 | **M** 13 |
| **N** 14 | **O** 15 | **P** 16 | **Q** 17 | **R** 18 | **S** 19 | **T** 20 | **U** 21 | **V** 22 | **W** 23 | **X** 24 | **Y** 25 | **Z** 26 |

## 3. Adani ayesa kunyenga ndi kuopsa Nehemiya

**Nehemiya 6.1-19**

1Kunali tsono, atamva Sanibalati, ndi Tobiya, ndi Gesemu M-arabu, ndi adani athu otsala, kuti ndidatha kumanga lingali, posatsalaponso popasuka; (ngakhale pajapo sindinaika zitseko pazipata);
2anatumiza mau kwa ine Sanibalati ndi Gesemu, kuti, Tiyeni tikomane ku midzi ya ku cigwa ca Ono; koma analingirira za kundicitira coipa.
3Ndipo ndinawatumizira mithenga, ndi kuti, Ndirikucita nchito yaikuru, sindikhoza kutsika; ndiidulirenji padera nchito poileka ine, ndi kukutsikirani? 4Nanditumizira ine mau otere kanai; ndinawabwezeranso mau momwemo. 5Pamenepo Sanibalati anatuma mnyamata wace kwa ine kacisanu, ndi kalata wosatseka m'dzanja mwace;
6m'menemo mudalembedwa, Kwamveka mwa amitundu, ndi Gasimu acinena, kuti iwe ndi Ayuda mulikulingirira za kupanduka; cifukwa cace mulikumanga lingali; ndipo iwe udzakhala mfumu yao monga mwa mau awa. 7Ndiponso waika aneneri akubukitsa za iwe ku Yerusalemu, ndi kuti, Ku Yuda kuli mfumu, ndipo zidzamveka kwa mfumu, kuti kuli zotere. Tiyeni tsono tipangane pamodzi.
8Koma ndinamtumizira mau, akuti, Palibe zinthu zotere zonga unenazi, koma uzilingirira mumtima mwako.
9Pakuti anafuna onse kutiopsa, ndi kuti, Manja ao adzaleka nchito, ndipo siidzacitika. Koma Inu, Mulungu, mulimbitse manja anga tsopano.
10Pamenepo ndinalowa m'nyumba ya Semaya mwana wa Delaya, mwana wa Mehetabele, wobindikizidwayo, ndipo anati, Tikomane ku nyumba ya Mulungu m'kati mwa Kacisi, titsekenso pa makomo a Kacisi; pakuti akudza kudzapha iwe, inde akudza usiku kudzapha iwe.
11Koma ndinati, Munthu ngati ine nkuthawa kodi? ndani wonga ine adzalowa m'Kacisi kupulumutsa moyo wace? sindidzalowamo.
12Ndipo ndinazindikira kuti sanamtuma Mulungu; koma ananena coneneraco pa ine, popeza Tobiya ndi Sanibalati adamlembera.
13Anamlembera cifukwa ca ici, kuti ine ndicite mantha, ndi kucita cotero, ndi kucimwa; ndi kuti anditolerepo mbiri yoipa ndi kundinyoza.
14Mukumbukile, Mulungu wanga, Tobiya ndi Sanibalati monga mwa nchito zao izi, ndi Nowadiya mneneri wamkazi yemwe, ndi aneneri otsala, amene anafuna kundiopsa.

15Ndipo linga linatsirizika pa tsiku la makumi awiri ndi lacisanu la mwezi wa Eluli, titalimanga masiku makumi asanu mphambu awiri.
16Ndipo kunali atacimva adani athu onse, amitundu onse akutizinga anaopa, nagwadi nkhope; popeza anazindikira kuti nchitoyi inacitika ndi Mulungu wathu.
17Masikuwo aufulu a Yuda analemberanso akalata ambiri kwa Tobiya; ndipo anawafikanso akalata ace a Tobiya.
18Pakuti ambiri m'Yuda analumbirirana naye cibwenzi; popeza ndiye mkamwini wace wa Sekaniya mwana wa Ara; ndi mwana wace Yehohanana adadzitengera mwana wamkazi wa Mesulamu mwana wa Berekiya.
19Anachulanso nchito zace zokoma pamaso panga namfotokozera iye mau anga. Ndipo Tobiya anatumiza akalata kuti andiopse ine.

**Nehemiya 12.27, 30, 31, 38, 40, 43**

27Ndipo popereka linga la Yerusalemu anafunafuna Alevi m’malo mwao monse, kubwera nao ku Yerusalemu, kuti acite kuperekaku mokondwera, ndi mayamiko, ndi kuyimbira, ndi nsanje, zisakasa, ndi azeze.
(…)
30Ndipo ansembe ndi Alevi anadziyeretsa okha, nayeretsa anthu, ndi zipata, ndi linga.
31Pamenepo ndinakwera nao akuru a Yuda pa lingali, ndinaikanso oyamikira magulu awiri akuru oyenda molongosoka; lina loyenda ku dzanja lamanja palinga kumka ku cipata ca kudzala;
(…)
38Ndi gulu lina la oyamikira linamuka mokomana nao, ndi ine ndinawatsata, pamodzi ndi limodzi la magawo awiri la anthu palinga, napitirira pa nsanja ya ng’anjo, mpaka ku linga lacitando.
(…)
40Atatero, magulu awiriwo a iwo oyamikira anaima m’nyumba ya Mulungu, ndipo ine ndi limodzi la magawo awiri a olamulira pamodzi ndi ine.
(…)
43Ndipo anaphora nsembe zambiri tsiku lija, nasekerera; pakuti Mulungu anawakondweretsa ndi cimwemwe cacikuru; ndi akazi omwe ndi ana anakondwera; ndi cikondwerero ca Yerusalemu cinamveka kutali.

**Mafunso**

1. Kodi Sanibalati ndi Gesemu anafuna kucita ciani kulingana ndi Nehemiya 6.2?
2. Kodi Nehemiya anawayankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Sanibalati analemba kalata kwa Nehemiya. Kodi analemba ciani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Kulingana ndi ndime ya 10, adani anapanga ciwembu cina. Kodi anapanga ciwembu cotani? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Kodi Nehemiya anayankha bwanji? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Kodi tiyenera kucita ciani pamene anthu ena afuna kuti ticimwe?
8. Kodi Ayuda anapereka bwanji linga la Yerusalemu kwa Mulungu kulingana ndi ndime za m'Nehemiya 12?
9. Ansembe ndi Alevi anadziyeretsa. Ici cinali cizindikiro kuti ayenera kukhala oyera kuti atumikire Mulungu. Nanga ife, tingakhale bwanji oyera pa maso pa Mulungu?
10. Anthu anamulemekeza Mulungu cifukwa ca zimene anawacitira. Kodi Mulungu anaticitira ciani? Kodi mumalemekeza Mulungu cifukwa ca zimene anakucitirani ndipo amakucitiranibe?

**Sewero**

Pezani mau onse

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| I | T | A | L | A | B | I | N | A | S |
| S | O | N | U | N | L | W | A | C | E |
| I | B | A | G | I | N | E | E | E | K |
| C | I | H | N | G | A | T | I | E | A |
| A | Y | G | U | T | A | L | A | K | N |
| K | A | M | L | I | A | D | A | N | I |
| Y | U | F | U | L | I | A | D | U | Y |
| A | U | A | M | A | K | O | M | O | A |

| | |
|---|---|
| Sanibalati | Tobiya |
| linga | Mulungu |
| kalatu | Kacisi |
| wace | Sekaniya |
| ine | ngati |
| makomo | Yuda |
| adani | ufulu |
| ana | ace |

# 4. Tsiku la Sabata likhalanso lopatulika

**Nehemiya 13**
1Tsiku lomwelo anawerenga m'buku la Mose m'makutu a anthu, napeza m'menemo kuti Aamoni ndi Amoabu asalowe mu msonkhano wa Mulungu ku nthawi yonse;
2popeza sanawacingamira ana a Israyeli ndi cakudya ndi madzi, koma anawalemberera Balamu awatemberere; koma Mulungu wathu anasanduliza tembererolo likhale mdalitso.
3Ndipo kunali, atamva cilamuloco, anasiyanitsa pa Israyeli anthu osokonezeka onse.
4Cinkana ici, Eliasibu wansembe, woikidwa asunge zipinda za nyumba ya Mulungu wathu, anacita cibale ndi Tobiya,
5namkonzera cipinda cacikuru, kumene adasungira kale zopereka za ufa, libano, ndi zipangizo, ndi limodzi limodzi la magawo khumi a tirigu, vinyo, ndi mafuta, zolamutidwira Alevi, ndi oyimbira, ndi odikira, ndi nsembe zokweza za ansembe.
6Koma pocitika ici conse sindinakhala ku Yerusalemu; pakuti caka ca makumi atatu ndi caciwiri ca Aritasasta mfumu ya Babulo ndinafika kwa mfumu, ndipo atapita masiku ena ndinapempha mfumu indilole;
7ndipo ndinafika ku Yerusalemu, ndi kuzindikira coipa anacicita Eliasibu, cifukwa ca Tobiya, ndi kumkonzera cipinda m'mabwalo a nyumba ya Mulungu.
8Ndipo ndinaipidwa naco kwambiri, motero ndinataya kubwalo akatundu onse a m'nyumba ya Tobiya, kuwacotsa m'cipindamo.
9Pamenepo ndinalamulira, ndipo anayeretsa zipindazo; ndipo ndinabwezeramonso zipangizo za nyumba ya Mulungu, pamodzi ndi zopereka za ufa ndi libano.
10Ndinazindikiranso kuti sanapereka kwa Alevi magawo ao; m'mwemo Alevi ndi oyimbira adathawira yense ku munda wace.
11Potero ndinatsutsana nao olamulira, ndinati, Yasiyidwiranji nyumba ya Mulungu? Ndipo ndinawasonkhanitsa, ndi kuwafka m'malo mwao.
12Ndi Ayuda onse anabwera nalo limodzi limodzi la magawo khumi a tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta, ku nyumba za cuma.
13Ndinaikanso osunga cuma, asunge nyumba za cuma: Selemiya wansembe, ndi Zadoki mlembi; ndi wa Alevi, Pedaya; ndi wakuwathandiza, Hanani mwana wa Zakuri, mwana wa Mataniya; popeza anayesedwa okhulupirika ndi udindo wao, ndiwo kugawira abale ao.

14Mundikumbukile Mulungu wanga mwa ici, nimusafafanize zokoma zanga ndinazicitira nyumba ya Mulungu wanga, ndi maudikiro ace.
15Masiku awa ndinaona ku Yuda ena akuponda mphesa m'coponderamo dzuwa la Sabata, ndi akubwera nayo mitolo ya tirigu, ndi kuisenzetsa pa aburu; momwemonso vinyo, mphesa, ndi nkhuyu, ndi zosenza ziri zonse, zimene analowa nazo m'Yerusalemu dzuwa la Sabata, ndipo ndinawacitira umboni wakuwatsutsa tsikuti anagulitsa zakudya.
16Anakhalanso m'menemo a ku Turo, obwera nazo nsomba, ndi malonda ali onse, nagulitsa dzuwa la Sabata kwa ana a Yuda ndi m'Yerusalemu.
17Pamenepo ndinatsutsana nao aufulu a Yuda, ndinanena nao, Cinthu canji coipa ici mucicita, ndi kuipsa naco dzuwa la Sabata? ‘
18Sanatero kodi makolo anu, ndipo Mulungu wathu anatifikitsira ife ndi mudzi uno coipa ici conse? koma inu muonjezera Israyeli mkwiyo pakuipsa Sabata.
19Ndipo kunali, kukadayamba cizirezire pa zipata za Yerusalemu, losafika Sabata, ndinawauza atseke pamakomo; ndinawauzanso kuti asatsegulepo, koma litapita Sabata ndipo; ndipo ndinaimika anyamata anga ena pazipata, kuti pasalowe katundu dzuwa la Sabata.
20Momwemo eni malonda ndi ogulitsa malonda ali onse, anagona kunja kwa Yerusalemu kamodzi kapena kawiri.
21Koma ndinawacima umboni wakuwatsutsa, ndinanena nao, Mugoneranji pafupi pa linga? mukateronso ndikuthirani
manja. Kuyambira pomwepo sanafikanso pa Sabata. 22Ndipo ndinauza Alevi kuti adziyeretse, nabwere, nasunge
pazipata kupatula dzuwa la Sabata. Mundikumbukire Icinso, Mulungu wanga, ndi kundileka monga mwa cifundo canu cacikuru.
23Masiku aja ndinaonanso Ayudawo anadzitengera akazi a Asidodi, Aamoni, ndi Amoabu,
24ndi ana ao analankhula mwina Ciasidodi, osadziwitsa kulankhula Ciyuda, koma monga umo amalankhula mtundu wao uli wonse.
25Ndipo ndinatsutsana nao, ndi kuwatemberera, ndi kukantha ena a iwo, ndi kumwetula tsitsi lao, ndi kuwalumbiritsa pa Mulungu ndi kuti, Musapereka ana anu akazi kwa ana ao amuna, kapena kutengera ana anu amuna, kapena a inu nokha, ana ao akazi.

26Nanga Solomo mfumu ya Israyeli sanacimwa nazo zinthu izi? cinkana mwa amitundu ambiri panalibe mfumu ngati
iye, ndi Mulungu wace anamkonda, ndi Mulungu wace anamlonga mfumu ya Aisrayeli onse; koma ngakhale iye, akazi
acilendo anamcimwitsa.
27Ndipo kodi tidzamvera inu, kucita coipa ici cacikuru conse, kulakwira Mulungu wathu ndi kudzitengera akazi
acilendo?
28Koma wina wa ana a Yoyada, mwana wa Eliasibu mkuru wa ansembe, anali mkamwini wa Sanibalati Mhoroni;
cifukwa cace ndinampitikitsa kumcotsa kwa ine.
29Muwakumbukile Mulungu wanga, popeza anadetsa unsembe, ndi pangano la unsembe, ndi la Alevi.
30Momwemo ndinawayeretsa kuwacotsera acilendo onse, ndi kuikira udikiro ansembe ndi Alevi, yense ku nchito yace;
31ndi copereka ca nkhuni pa nthawi zoikika, ndi wa zipatso zoyamba. Mundikumbukile, Mulungu wanga, cindikomere.

**Mafunso**

1. M'ndime ya 7 tawerenga za cinthu coipa. Ndi ciani cimene cinacitika?
2. Kodi Nehemiya anacita ciani atamva ico? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. M'ndime ya 10 tawerenga bvuto laciwiri limene Nehemiya anakomana nalo pamene anabweranso ku Yersualemu. Fotokozani bvuto iro.
4. Nanga ife, timathandiza anthu ena amene agwira nchito kwa Mulungu kuti nchito iyi ingapite patsogolo?
5. Kodi bvuto lacitatu linali lotani kulingana ndi ndime ya 15?
6. Kodi m'nthano iyi taphunzira ciani kulingana ndi kugwira nchito pa tsiku la Mulungu?
7. Kodi mumacita ciani pa tsiku la Mulungu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao.

| | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | |
| 11 | 21 | 13 | 22 | 5 | 18 | 1 |

| | | | | |
|---|---|---|---|---|
| | | | | |
| 14 | 4 | 9 | 11 | 15 |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |
| 11 | 15 | 16 | 15 | 19 | 1 |

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |
| 14 | 19 | 5 | 13 | 2 | 5 |

| | | | | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A 1 | B 2 | C 3 | D 4 | E 5 | F 6 | G 7 | H 8 | I 9 | J 10 | K 11 | L 12 | M 13 |
| N 14 | O 15 | P 16 | Q 17 | R 18 | S 19 | T 20 | U 21 | V 22 | W 23 | X 24 | Y 25 | Z 26 |

## Tipulumutseni, Yehova, Mulungu wathu, ndi kutisokolotsa kwa amitundu, kuti tiyamike dzina lanu loyera, ndi kudzitamandira naco cilemekezo canu – Salimo 106.47